

ANENERI A M'CHIPANGANO CHAKALE



Phunziro 3,
October 17, 2026



«Mmamawa,
ananyamuka kupita ku
chipululu cha Tekowa.
Akunyamuka, Yehosafati
anayimirira ndipo anati,
“Tandimverani ine anthu
a Yuda ndi Yerusalemu!


Khalani ndi
chikhulupiriro mwa
Yehova Mulungu wanu
ndipo
mudzatchinjirizidwa,
khalani ndi
chikhulupiriro mwa
aneneri ake ndipo
mudzapambana.”»

(2 Mbiri 20:20, cCL)

Mu nthawi ya Chipangano Chakale, anthu omwe amalandira mauthenga ochokera kwa Mulungu kuti alankhule ndi ena ankatchedwa alauli kapena aneneri (1 Samueli 9:9).

Anali ndi kuthekera kodziwa zinthu zobisika, ngakhaleenso zimene zidzachitike m'tsogolo (1 Samueli 9:6). Koma ntchito yawo sinali yongodziwa zinthu zimenezi zokha; inkaphatikizapo ntchito zina zambiri. Kuthekera kumeneku, ndithudi, sikunachokere kwa iwo okha, koma kwa Mulungu.

Koma panalinso aneneri onyenga amene ankalankhula za “Iwo akungoyankhula za masomphenya a m’mitima mwawo basi (Yeremiya 23:16).




- Kodi ndani amene anaitanidwa kugwira ntchito ya uneneri?**
- Kodi aneneri ankakhala ndi makhalidwe otani?**
- Kodi aneneri ankagwira ntchito zotani?**
- Kodi ndi akazi ati amene anali ndi mphatso ya uneneri?**
- Kodi aneneri onyenga anali ndi makhalidwe otani?**

KODI NDANI AMENE ANAITANIDWA KUGWIRA NTCHITO YA UNENERI?

"Eliya anali munthu ngati ife. Iye anapemphera mwamphamvu kuti mvula isagwe ndipo sinagwedi kwa zaka zitatu ndi theka." (Yakobo 5:17 CCL)


Tikhoza kulakwitsa poganiza kuti aneneri anali anthu apadera amene anali ndi mphamvu zoposa za anthu wamba. Koma Mose anapereka chifukwa chakuti sankatha kulankhula bwino (Eksodo 4:10); Yesaya ananena kuti anali ndi milomo yodetsedwa (Yesaya 6:5); ndipo Yeremiya ankadziona kuti anali wamng'ono kwambiri kuti agwire ntchito imeneyi (Yeremiya 1:6).

Eliya, amene analimba mtima kuchenjeza Mfumu Ahabu kuti kudzakhala chilala chachikulu chifukwa cha kusalemekeza Mulungu kwake, Baibulo limanena za iye kuti: "Anali munthu monga ife tomwe" (Yakobo 5:17).




Atachita chozizwitsa chachikulu, Eliya anataya mtima kwambiri chifukwa Mfumukazi Yezebeli anamuopseza kuti adzamupha (1 Mafumu 19:2-4).

Ndizodziwikiratu kuti Mulungu sasankha aneneri ake chifukwa chakuti ndi anthu angwiro. Nanga kodi amaona chiyani mwa iwo? Amaona chikondi chawo pa Mulungu ndi mtima wawo wofunitsitsa kumumvera.



KODI ANENERI ANKAKHALA NDI MAKHALIDWE OTANI?

"Koma Mikaya anati, ' Pali Yehova wamoyo, ine ndikawawuza zokhazo zimene Yehova akandiwuze' "
(1 Mafumu 22:14 CCL)




Monga anthu olankhulira Mulungu, aneneri aamuna ndi aakazi ankayesetsa kukhala m'moyo wogwirizana ndi kuitanidwa kwawo (1 Samueli 12:3-4). Anthu ankawadziwa monga "anthu a Mulungu" komanso "anthu olemekkezeka" (1 Samueli 9:6).

Anthu amene anakana kulandira uthenga wawo ankadana nawo ndipo ankawaopseza (1 Mafumu 22:8, 27). Koma ngakhale kuti ankakumana ndi mavuto ndi ziwopsezo zambiri, aneneriwo anapitirizabe kupereka uthenga wa Mulungu mokhulupirika.

Mikaya anaima pamaso pa mafumu awiri, aneneri 400 amene anali kupereka uthenga wokondweretsa mafumuwo, komanso mtumiki amene anamulangiza kuti alankhule mogwirizana ndi mmene zinthu zinaliri (1 Mafumu 22:10-13). Komabe, Mikaya anaima molimba mtima ndipo anakana kulankhula china chilichonse kupatulapo zimene Mulungu anamuwululira (1 Mafumu 22:14).

Sanali anthu angwiro, koma anali amuna ndi akazi okonda pemphero, okhulupirika pa Mawu a Mulungu, komanso odzipereka kutumikira Mulungu ndi anthu ake (1 Samueli 12:23; Yeremiya 42:4).



KODI ANENERI ANKAGWIRA NTCHITO ZOTANI?

"Ukadzozenso Yehu mwana wa Nimisi kuti akhale mfumu ya Israeli, ndiponso ukadzoze Elisa mwana wa Safati wa ku Abeli-Mehola kuti akhale mneneri wolowa m'malo mwako." (1 Mafumu 19:16)

Mwa zina, aneneri ankagwira ntchito zotsatirazi :



Kwa mafumu

- 👑 Ankawazodza
(1 Mafumu 19:16)
- 👑 Ankawalimbikitsa
akamachita
zabwino
(2 Mbiri 15:8)
- 👑 Ankawadzudzula
akamachita
zolakwika
(1 Mafumu 21:20)

Kwa ansembe

- 👑 Ankawadzudzula
akamachita
zolakwika
(Malaki 2:1-2)

Kwa anthu

- 👤 Ankawaphunzitsa
kuyenda m'njira za
Mulungu (Mika 6:8)
- 👤 Ankawauza
poyera za
machimo awo
(Yesaya 58:1)
- 👤 Ankawaitana kuti
alape machimo
awo (Ezekieli
18:32)


Kwa ife

- 📖 Analemba
mauthenga awo
(2 Mbiri 13:22)

KODI NDI AKAZI ATI AMENE ANALI NDI MPHATSO YA UNENERI?

"Debora, mneneri wamkazi, mkazi wake wa Rapidoti ndiye ankatsogolera Israeli nthawi imeneyo" (Oweruza 4:4)

Chipangano Chakale chimatchula akazi asanu amene ankatchedwa aneneri. Mmodzi mwa iwo, Nowadiya, anali mneneri wonyenga (Nehemiya 6:14). Ponena za wina, amene anali mkazi wa Yesaya, sitikudziwa ngati ankatchedwa mneneri chifukwa chakuti anali ndi mphatso ya uneneri, kapena chifukwa chakuti anali mkazi wa mneneri (Yesaya 8:3).



MIRIAM. Monga mneneri wamkazi, iye anatsogolera akazi poimba nyimbo atawoloka Nyanja Yofiira. Anathandizanso abale ake kutsogolera anthu pa ulendo wawo wodutsa mUchipululu (Eksodo 15:20; Mika 6:4).



DEBORA. Iye anali mneneri wamkazi komanso woweruza, ndipo pamodzi ndi Baraki anatsogolera anthu kunkhondo yolimbana ndi Sisera. Atapambana nkondoyo, anaimba nyimbo yauneneri yotamanda Mulungu (Oweruza 4:4-9; 5:1).



HUDA. Mfumu Yosiya inapita kwa iye kukafunsa za buku la Chilamulo limene linapezeka. Kuwonjezera pa kuyankha funso la mfumuyo, iye analankhulanso mawu achilimbikitso kwa mfumuyo (2 Mafumu 22:14-20).

KODI ANENERI ONYENGA ANALI NDI MAKHALIDWE OTANI?

"Ndipo Yehova anandiwuza kuti, "Ndi zabodza kuti aneneriwa akunenera m'dzina langa. Ine sindinawatume kapena kuwasankha kapenanso kuyankhula nawo. Iwo amakuwuzani zinthu zabodza zomwe amati anazona m'masomphenya, kapena pogwiritsa ntchito mawula achabechabe. Zimene amayankhula ndi zongopeka m'mutu mwawo.' " (Yeremiya 14:14)

Si onse amene ankalo sera amene ankachita zimenezi chifukwa chakuti analandira uthenga kuchokera kwa Mulungu (Yeremiya 14:14). Kodi uthenga wawo unali wotani, ndipo n'chifukwa chiyani ankaupereka?

Ankapeka ulosi wawo wa m'mutu mwawo (Ezekieli 13:2, 17)

Ankanena zimene anthu ankafuna kumva (Ezekieli 13:16)

Sankadzudzula machimo a anthu (Ezekieli 13:22)

Ankafuna kudzipezera phindu lawo iwo eni (Ezekieli 13:19)

Chifukwa chiyani munthu anganene kuti akulankhula m'malo mwa Mulungu pamene akudziwa kuti sizoonanso? Kudzinyenga? Kufuna kutchuka, kapena kufuna phindu la ndalama kapena zina?

Chinthu chomvetsa chisoni kwambiri ndi aneneri onyenga nchakuti pali anthu amene amawamvera ndi kuwatsatira. Amakonda zomwe amalankhula chifukwa sizifuna kuti asinthe moyo wawo, komanso sizimawadzutsa chikumbumtima kuti azindikire zolakwa zawo. Koma kutsatira njira yawo kumangowatsogolera ku imfa.

Mneneri woota nthawi zonse amachenjeza anthu za kuopsa kwa uchimo, ndipo amawalimbikitsa kukhala okhulupirika kwa Mulungu, mosasamala kanthu za mavuto amene angakumane nawo.



“Palibe mtumwi kapena mneneri amene ananenapo kuti anali wopanda uchimo. Anthu amene adakhala pafupi kwambiri ndi Mulungu, amene anali okonzeka kutaya ngakhale moyo wawo m'malo mochita choipa mwadala, komanso amene Mulungu adawawonetsera kuwala ndi mphamvu zakumwamba, anavomereza kuchimwa kwawo mwachibadwidwe. Sanadalire mphamvu zawo monga anthu, kapena kudziyesa olungama mwa iwo okha, koma anadalira kwathunthu chilungamo cha Khristu.”

EGW (The Acts of the Apostles, p. 561)

ZOWONJEZERA : KUITANIDWA KWA ELLEN G. WHITE KUKHALA MNENERI

Atalandira masomphenya ake oyamba, Ellen ankaona kuti sanali wokonzeka mokwanira kugwira ntchito yake ya uneneri. Chifukwa cha kudwaladwala komanso maphunziro ake ochepa, Ellen, yemwe anali ndi zaka 17, ankadziona kuti sanali woyenera ndipo analibe kuthekera kokwaniritsa ntchito imene Mulungu anamuitanira.

Patapita sabata imodzi kuchokera pamene anaona masomphenya ake oyamba, Ellen anaonanso masomphenya achiwiri, amene anamuchenjeza za mavuto amene adzakumane nawo. Atapemphera kwambiri, komanso kulimbikitsidwa ndi abale ndi alongo ena m'chikhulupiriro, Ellen pamapeto pake anavomera kuitanidwa kwake ndi Mulungu.

M'zaka zochepera makumi awiri, atalandira masomphenya ambiri komanso mothandizidwa ndi mwamuna wake, James White, Ellen anathandiza kukhazikitsa maziko a Mpingo wa Seventh-day Adventist, umene unakhazikitsidwa mwalamulo m'chaka cha 1863).



Utumiki wake unathandiza kwambiri kukhazikitsa ntchito za zaumoyo ndi maphunziro za Mpingo wa Adventist. Anasiyanso zolembe zouziridwa ndi Mulungu zokwana pafupifupi masamba 100,000, zimene zikupitirizabe kupereka malangizo ochokera kwa Mulungu kwa anthu padziko lonse lapansi.

